14. Dzuwa lingawale mwaubwino ndi kufunditsa dziko lapansi.
15. Koma usiku dzuwa siliwala. Kenaka kuli mdima.
16. Ambuye apanganso magetsi usiku: mwezi ndi nyenyezi.
17. Pa tsiku lacisanu Mulungu akuti: 'Ndifuna nsomba m'madzi.'
Funso: Kodi Mulungu anati ciani pa tsiku lacisanu?
Yankho: Ndifuna nsoma m'madzi.
18. Nsomba zazikulu ndi zazing'ono.
19. M'mlengalenga Ambuye apanga mbalame. Mbalame za mitundu yambiri.
20. Mulungu apanganso nyama pa dziko.
Funso: Ndani amene analenga nyama?
Yankho: Mulungu
21. Izi zicitika pa tsiku lacisanu ndi cimodzi.
22. Nyama zazikulu ndi zazing'ono. Mvu ndi akalulu. Mkango ndi nkono.
23. Ati kukoma m'mene Ambuye anapangira zonse!
24. Cothera cimene Mulungu apanga ndi munthu. Amuitana dzina lake Adamu.
Funso: Kodi dzina la munthu woyamba linali ciani?
Yankho: Adamu.
25. Adamu ayenera kupatsa nyama zonse maina.
Funso: Kodi Adamu anacita ciani?
Yankho: anapatsa nyama zonse maina.
26. Nyama zonse zili pamodzi: yaimuna ndi yaikazi.
27. Koma Adamu ali yekha. Ndipo Ambuye ampatsa Adamu mkazi.
Funso: Ndani amene anapatsa Adamu mkazi wace?
Yankho: Ambuye (Mulungu)
28. Dzina lake ndi Hava. Cikondwerero kwa Adamu!

Nthano iyi ipezeka mu Genesis 1 ndi 2

Phunziro 33b				
a	e	i	o	u
ba	be	bi	bo	bu
bva	bve	bvi	bvo	bvu
bwa	bwe	bwi	bwo	bwu
ca	ce	ci	co	cu
cha	che	chi	cho	chu
da	de	di	do	du
dwa	dwe	dwi	dwo	dwu
dya	dye	dyi	dyo	dyu
dza	dze	dzi	dzo	dzu
fa	fe	fi	fo	fu
ga	ge	gi	go	gu
gwa	gwe	gwi	gwo	gwu
ha	he	hi	ho	hu
ja	je	ji	jo	ju
ka	ke	ki	ko	ku
kha	khe	khi	kho	khu
kwa	kwe	kwi	kwo	kwu
la	le	li	lo	lu
ma	me	mi	mo	mu
mba	mbe	mbi	mbo	mbu
mca	mce	mci	mco	mcu
mda	mde	mdi	mdo	mdu
mdza	mdze	mdzi	mdzo	mdzu
mfa	mfe	mfi	mfo	mfu
mka	mke	mki	mko	mku
mkha	mkhe	mkhi	mkho	mkhu
mkwa	mkwe	mkwi	mkwo	mkwu
mla	mle	mli	mlo	mlu
mna	mne	mni	mno	mnu
mpa	mpe	mpi	mpo	mpu
mpha	mphe	mphi	mpho	mphu
msa	mse	msi	mso	msu
mta	mte	mti	mto	mtu
mtsa	mtse	mtsi	mtso	mtsu
mva	mve	mvi	mvo	mvu

mwa	mwe	mwi	mwo	mwu
mza	mze	mzi	mzo	mzu
na	ne	ni	no	nu
ncha	nche	nchi	ncho	nchu
nda	nde	ndi	ndo	ndu
ndwa	ndwe	ndwi	ndwo	ndwu
nga	nge	ngi	ngo	ngu
ng'a	ng'e	ng'i	ng'o	ng'u
ngwa	ngwe	ngwi	ngwo	ngwu
nja	nje	nji	njo	nju
nka	nke	nki	nko	nku
nkha	nkhe	nkhi	nkho	nkhu
nkha	nkhe	nkhi	nkho	nkhu
nkha	nkhe	nkhi	nkho	nkhu
nsa	nse	nsi	nso	nsu
ntha	nthe	nthi	ntho	nthu
nya	nye	nyi	nyo	nyu
nza	nze	nzi	nzo	nzu
pa	pe	pi	po	pu
pha	phe	phi	pho	phu
psa	pse	psi	pso	psu
pwa	pwe	pwi	pwo	pwu
ra	re	ri	ro	ru
sa	se	si	so	su
sha	she	shi	sho	shu
swa	swe	swi	swo	swu
ta	te	ti	to	tu
tha	the	thi	tho	thu
thya	thye	thyi	thyo	thyu
tsa	tse	tsi	tso	tsu
va	ve	vi	vo	vu
wa	we	wi	wo	wu
ya	ye	yi	yo	yu
za	ze	zi	zo	zu

Aa Bb Cc Dd Ee Ff Gg Hh Ii Jj Kk Ll Mm Nn Oo Pp Rr Ss Tt Uu Vv Ww Yy Zz

a = ɑ g = ɢ

Phunziro 34 – Mayeso ndi kuwerenga momvetsa

- 1. Funsani aphunzi ngati kuli bvuto limene ali nayo pa nkhani ya kuwerenga ndi kulemba**
- 2. Uzani aphunzi kulemba mau awa m'mabuku ao.**
ana, kena, make, msanga, mwamuna, kwina, Yesu, nsomba, atumwi, ifenso, nyumba, ndalama, ndani, nthano, kumenya, mwezi, thupi, pang'ono, moto, tsopano, madzi, anga, mtengo, mwana, kusunkhana, zikomo, pepani, mphamvu, uci, bedi, njinga, bwino, fulumira, bwanji, ciani, ng'anga
- 3. Tengani mabuku ao ndipo konzani zolakwika zao**
- 4. Fotokozaninso malembo ndi masilabi omwe aphunzi sanalembe bwino**
- 5. Werenganinso pepala Phunziro 33a ndipo funsani aphunzi mafunso opezeka pa pepala Phunziro 33a m'buku la mphunzitsi.**
- 6. Tsirizani phunziro pa kuimba nyimbo**

Nchito ya kunyumba: werengani pepala Phunziro 34 kunyumba. Uzani kudula mau m'masilabi ngati alephera kuwawerenga. Ngati simukhoza kuwatengera pepala, lembani mau ena pa bolodi ndipo lolani aphunzi kuwawerenga kunyumba.

Phunziro 34

- | | | |
|--------------------|-----------------------|--------------------|
| 1. ndondomeko | 2. madalitso | 3. zokondweretsa |
| 4. umphawi | 5. cilengedwe | 6. nyamalikiti |
| 7. zazing'ono | 8. sitinayende | 9. kuyendayenda |
| 10. zinalengedwa | 11. adzadziphatika | 12. wolakalakika |
| 13. yotembereredwa | 14. mudzabwerera | 15. ndidzabisika |
| 16. mgwirizano | 17. kumtamandira | 18. asanabadwe |
| 19. mwamvetsetsa | 20. anamizidwa | 21. sadzaononganso |
| 22. wolunjika | 23. utawaleza | 24. kupulumutsidwa |
| 25. anasankhidwa | 26. adakwatirana | 27. akubvutitsani |
| 28. anayanjananso | 29. citanthauzo | 30. mungalandire |
| 31. wolemekezeka | 32. kudzicepetsa | 33. lapamwamba |
| 34. coledzeretsa | 35. anadzibvumbulutsa | 36. mnyamatayo |

Phunziro 35 – kuwerenga ndi kulemba

1. Lembani pa bolodi ndipo werengani pamodzi

a	e	i	o	u
ba	ce	di	fo	gu
ha	che	ji	ko	khu
la	me	mbi	mko	nu
nda	nge	ng'i	njo	nku
nkha	pe	phi	mpo	mphu
ra	se	msi	nso	tu
tha	tse	nthi	mto	vu
bva	mve	wi	bwo	dwu
gwa	kwe	mwi	yo	dyu
nya	ze	dzi	nzo	

2. Werengani pepala Phunziro 34 pamodzi

3. Uzani aphunzi kulemba ziganizo izi m'mabuku ao

1. Mulungu analenga Adamu ndi Hava.
2. Anthu sanakhulupirire Nowa pamene anamanga combo.
3. Mulungu afuna anthu kumumvera.
4. Yosefe amanga nyumba mosungira zakudya.
5. Nyama zonse zinafa mwadzidzidzi.
6. Ambuye Yesu anafa pa mtanda.
7. Davide anakonda kuimba zeze lake.
8. Danieli anaponyedwa mu dzenje la mikango.
9. Yesu anaciritsa anthu ambiri.
10. Aona ng'ombe zazikazi zisanu ndi ziwiri zonenepa.

4. Tengani mabuku ao ndipo konzani zolakwika zao

5. Tsirizani phunziro pa kuimba nyimbo

Nchito ya kunyumba: lembani nkhanu imene icitika ku Petauke (tsamba limodzi)

Phunziro 36 – Kuwerenga momvetsa

1. Congani nchito yao ya kunyumba ndipo konzani zolakwika

2. Lembani pa bolodi ndipo werengani pamodzi

me	se	dyu	o	mphu
njo	tse	msi	nku	dwu
e	mto	ha	ng'i	yo
ra	nthi	ba	nzo	tu
nu	bva	tha	gu	mko
phi	nda	ce	nge	khu

3. Uzani aphunzi kulemba masilabi awa pa bolodi

mve	che	ji	fo	dzi
mpo	vu	u	kwe	a
pe	mwi	nya	bwo	nso
la	se	di	mbi	wi
gwa	ko	ze	i	nkha

4. Werengani pamodzi pepala Phunziro 36 ndipo funsani mafunso opezeka pa pepala Phunziro 36 m'buku la mphunzitsi.

Ngati simukhoza kuwatengera pepala, lembani ziganizo 1-26 pa bolodi, lolani aphunzi kulemba ziganizo izi m'mabuku ao ndipo funsani mafunso 1-9 cabe.

5. Tsirizani phunziro pa kuimba nyimbo

Nchito ya kunyumba: werenganinso pepala Phunziro 36

Phunziro 36 (aphunzitsi cabe)

1. Tsiku lina Hava aona njoka.
2. M'njoka muli satana.

Funso: Kodi m'kati mwa njoka munali yani?

Yanko: Satana

3. Afunsa: 'Kodi sanakuloleni kudya zocokera ku mitengo?'
4. 'Inde anatilola,' atero Hava.
5. 'Kucokera ku mitengo yonse, kucotsako umodzi.
6. Ngati tikudya zocokera ku mtengo uja, tidzafa.'

Funso: Kodi ndi ciani cidzacitike ngati adzadya zocokera ku mtengo uja?

Yanko: Adzafa.

7. Koma njoka ikuti: 'Simudzafa.
8. Ngati mukudya zocokera kumtengo uja, mudzalingana ndi Mulungu yemwe.

Funso: Kodi adzakhala bwanji ngati adzadya zocokera ku mtengo uja?

Yanko: Adzalingana ndi Mulungu yemwe.

9. Hava apenya mtengo. Zipatso zioneke zokoma!
10. Akhulupirira zimene satana anena.
11. Hava atenga cipatso cimodzi ndipo acidya.

Funso: Kodi Hava anachita ciani?

Yanko: Hava anatenga cipatso cimodzi ndipo anacidya

12. Pambuyo pake apatsa cimodzi mwa zipatso kwa Adamu.
13. Adamu nayenso acidya. O! Tsoka.
14. Tsopano Adamu ndi Hava akhala osamvera.

Funso: Who have disobeyed the Lord?

Kodi ndani sanamvere Mulungu?

Yanko: Adamu ndi Hava.

15. Adamu ndi Hava akhala ndi mantha aakulu.
16. Mwadzidzidzi aona kuti ndi osabvala zobvala.
17. Athyola masamba kucokera ku mitengo ndi kupanga zobvala.
18. Abisala m'zisamba.

Funso: Kodi iwo anabisala kuti?

Yanko: M'zisamba.

19. Pambuyo pake akumva mau a Ambuye: 'Adamu uli kuti?'
20. Koma Adamu akhala ndi mantha kuopa Mulungu.
21. 'Kodi wadya zocokera ku mtengo uja?' 'Inde,' anena Adamu,
22. 'Koma, ndi cifukwa ca Hava.'

Funso: Kodi Adamu anaika mlandu pa yani?

Yanko: Hava

- 23 'Si zoona,' anena Hava. 'Njoka inandinyenga.'

Funso: Kodi Hava anaika mlandu pa yani?

Yanko: Njoka

24. Tsopano Adamu ndi Hava ayenera kucoka m'paradiso.
25. Ambuye awapatsa zobvala.
26. Zobvala zopangidwa kucokera ku zikopa za nyama.

Funso: Kodi zobvala zinapangidwo ndi ciani?

Yanko: Zikopa za nyama

27. Saloledwa kukhalanso m'munda muja.

- 28. Adamu ndi Hava ndi osakondwa!
- 29. Akhala osamvera.
- 30. Adamu ndi Hava ayenera cilango.
- 31. Ayenera kufa

Funso: Kodi cifukwa ciani Adamu ndi Hava anayenera kufa?

Yanko: Anakhala osamvera

- 32. Koma Mulungu adzakhululukira macimo a Adamu ndi Hava.
- 33. Mulungu alonjeza kutuma mwana wake.

Funso: Kodi Mulungu analonjeza ciani?

Yanko: Mulungu analonjeza kutuma Mwana wake.

- 34. Ambuye Yesu adzatenga cilango.
- 35. Ici cibweza cimwemwe ca Adamu ndi Hava.
- 36. Mulungu ndi wabwino!
- 37. Kucokera tsopano Adamu ndi Hava ayenera kugwira nchito ndi mphamvu.
- 38. Agwira nchito m'munda.
- 39. Nthawi zina atopa ndi kudwala.
- 40. Ici ndi cifukwa ca ucimo.

Funso: Kodi cifukwa ciani Adamu ndi Hava anadwala nthawi zina?

Yanko: Ici ndi cifukwa ca ucimo.

- 41. Adamu ndi Hava naonso akhala ndi ana: Kaini ndi Abele.

Funso: Kodi maina a ana a Adamu ndi Hava anali ciani

Yanko: Kaini ndi Abele.

Nthano iyi ipezeka mu Genesis 3

Phunziro 36 (ophunzira)

1. Tsiku lina Hava aona njoka.
2. M'njoka muli satana.
3. Afunsa: 'Kodi sanakuloleni kudya zocokera ku mitengo?'
4. 'Inde anatilola,' atero Hava.
5. 'Kucokera ku mitengo yonse, kucotsako umodzi.
6. Ngati tikudya zocokera ku mtengo uja, tidzafa.'
7. Koma njoka ikuti: 'Simudzafa.
8. Ngati mukudya zocokera kumtengo uja, mudzalingana ndi Mulungu yemwe.
9. Hava apenya mtengo. Zipatso zioneke zokoma!
10. Akhulupirira zimene satana anena.
11. Hava atenga cipatso cimodzi ndipo acidya.
12. Pambuyo pake apatsa cimodzi mwa zipatso kwa Adamu.
13. Adamu nayenso acidya. O! Tsoka.
14. Tsopano Adamu ndi Hava akhala osamvera.
15. Adamu ndi Hava akhala ndi mantha aakulu.
16. Mwadzidzidzi aona kuti ndi osabvala zobvala.
17. Athyola massamba kucokera ku mitengo ndi kupanga zobvala.
18. Abisala m'zisamba.
19. Pambuyo pake akumva mau a Ambuye: 'Adamu uli kuti?'
20. Koma Adamu akhala ndi mantha kuopa Mulungu.
21. 'Kodi wadya zocokera ku mtengo uja?' 'Inde,' anena Adamu,
22. 'Koma, ndi cifukwa ca Hava.'
23. 'Si zoona,' anena Hava. 'Njoka inandinyenga.'
24. Tsopano Adamu ndi Hava ayenera kucoka m'paradiso.
25. Ambuye awapatsa zobvala.
26. Zobvala zopangidwa kucokera ku zikopa za nyama.
27. Saloledwa kukhalanso m'munda muja.
28. Adamu ndi Hava ndi osakondwa!
29. Akhala osamvera.
30. Adamu ndi Hava ayenera cilango.
31. Ayenera kufa
32. Koma Mulungu adzakhululukira macimo a Adamu ndi Hava.
33. Mulungu alonjeza kutuma mwana wake.
34. Ambuye Yesu adzatenga cilango.
35. Ici cibweza cimwemwe ca Adamu ndi Hava.
36. Mulungu ndi wabwino!
37. Kucokera tsopano Adamu ndi Hava ayenera kugwira nchito ndi mphamvu.
38. Agwira nchito m'munda.
39. Nthawi zina atopa ndi kudwala.
40. Ici ndi cifukwa ca ucimo.
41. Adamu ndi Hava naonso akhala ndi ana: Kaini ndi Abele.

Nthano iyi ipezeka mu Genesis 3

Phunziro 37 – Kuwerenga

- 1. Uzani aphunzi kulemba masilabi awa m'mabuku ao**
ni, ta, bvo, mki, nje, gu, fa, ng'a, pu, mwa, dya, nze, nso, fi, le, mba, ro, msa, mpha, be, nku, gwa
- 2. Lembani masilabi pa bolodi ndipo lolani aphunzi kukonza zolakwika zao.**
- 3. Werengani pamodzi papala Phunziro 37.** Funsani aphunzi mafunso opezeka pa pepala Phunziro 37 m'buku la mphunzitsi. Ngati simukhoza kuwatengera pepala, lembani ziganizo 1-29 pa bolodi, werengani pamodzi ndipo lolani aphunzi kulemba ziganizo izi m'mabuku ao.
- 4. Tsirizani phunziro pa kuimba nyimbo.**
- 5. Nchito ya kunyumba:** werenganinso pepala Phunziro 37 ndipo ikani zizindikiro pa mau obvutitsa.

Phunziro 37 (Aphunzitsi cabe)

1. Mu Nazareti akhala Mariya.
2. Adzakwatira Yosefe.

Funso: Kodi Mariya anakhala kuti?

Yanko: Ku Nazareti.

3. Tsiku lina Mariya aona kuwala kwakukulu.
4. Ndi mngelo wocokera kuMwamba.
5. 'Usaope, Mariya,' anena mngelo.
6. 'Ndibweretsa uthenga wabwino.
7. Udzakhala ndi mwana. Ndiye Mwana wa Mulungu.'

Funso: Kodi mngelo anali ciani kwa Mariya?

Yanko: Usaope, Mariya. Ndibweretsa uthenga wabwino. Udzakhala ndi mwana. Ndiye Mwana wa Mulungu.

8. Yosefe ndi Mariya ayenera kupita ku Betlehemu.
9. Ici ndi cifuniro ca Kaisara Augusto.

Funso: Kodi dzina la Kaisara ndi ciani?

Yanko: Kaisara Augusto.

10. Ndi ulendo wautali umene ayenda.
11. Mariya akhala pang'ono kuona mwana!
12. Pothera afika m'Betlehemu.
13. Yosefe ndi Mariya ndi otopa cifukwa ca ulendo, koma kulibe malo kumene angagone.

Funso: Kodi Yosefe ndi Mariya anakomana bvuto lotani pakufika mu Betlehemu?

Yanko: Kulibe malo kumene angagone.

14. Ndipo mwana adzayenera kubadwira kuti?
15. Atafuna-funa nthawi yaitali apeza malo: m'khola la ng'ombe.
16. Umu ndiye m'mene Ambuye Yesu abadwira.
17. Mariya amuka Yesu m'nsalu
18. Nam'goneka modyerwa ng'ombe.

Funso: Kodi Mariya anacita ciani ndi Ambuye Yesu?

Yanko: Mariya amuka Yesu m'nsalu nam'goneka modyerwa ng'ombe.

19. Yosefe ndi Mariya ndi okondwera kwambiri.
20. Mulungu alonjeza Mwana uyu.
21. Ngakhale kwa Adamu ndi Hava.
22. Adzapulumutsa anthu ku macimo ao.

Funso: Kodi cifukwa nciani Ambuye Yesu anabadwa?

Yanko: Adzapulumutsa anthu ku macimo ao.

23. Onani, ndani awa?
24. Ndi abusa. Asamalira nkhosa. Ngakhale usiku.
25. Mwadzidzidzi abusa aona kuwala kwakukulu.
26. Ndi mngelo wocokera kuMwamba.
27. 'Ndibweretsa uthenga wacimwemwe cacikulu', atero mngelo

Funso: Kodi ndani amene anabweretsa uthenga wabwino?

Yanko: Ndi mngelo wocokera kuMwamba.

28. 'Ambuye Yesu wabadwa. M'khola la ng'ombe ku Betlehemu.
29. Agona modyerwa ng'ombe woikidwa m'nsalu.'

Funso: Kodi uthenga wabwino ndi ciani?

Yanko: Ambuye Yesu wabadwa.

30. Mwadzidzidzi muli angelo ambiri m'mlengalenga.

31. Aimba: Ulemerero kwa Mulungu ndi mtendere pansi pano.

Funso: Kodi angelo anaimba ciani?

Yanko: Ulemerero kwa Mulungu ndi mtendere pansi pano.

32. Cimveka bwino kwambiri!

33. Abusa ankhosa anena: 'Bwerani, tiyeni kwa Ambuye Yesu.'

34. Afika pakhola la ng'ombe.

35. Ndipo apeza Yosefe, Mariya ndi Mwana.

36. Abusa ankhosa atamanda Ambuye Yesu.

Funso: Kodi abusa anacita ciani?

Yanko: Anatamanda Ambuye Yesu.

37. Abusa alikufalitsa uthengawu paliponse.

38. 'Ambuye Yesu wabadwa, M'khola la ng'ombe ku Betelehemu.'

39. Koma anthu sakhulupirira ici.

Funso: Kodi anthu anakhulupirira uthenga wa azibusa?

Yanko: Anthu sanakhulupirire

40. Yosefe ndi Mariya acoka m'khola la ng'ombe.

41. Afuna nyumba m'Betelehemu.

42. Ndiye kumene Yosefe, Mariya ndi Ambuye Yesu adzakhala.

Funso: Kodi Yosefe, Mariya ndi Ambuye Yesu anakhala kuti?

Yanko: M'Betelehemu.

Nthano iyi ipezeka mu Luka 1. 26-38 ndi Luka 2. 1-21

Phunziro 37 (Ophunzira)

1. Mu Nazareti akhala Mariya.
2. Adzakwatira Yosefe.
3. Tsiku lina Mariya aona kuwala kwakukulu.
4. Ndi mngelo wocokera kuMwamba.
5. 'Usaope, Mariya,' anena mngelo.
6. 'Ndibweretsa uthenga wabwino.
7. Udzakhala ndi mwana. Ndiye Mwana wa Mulungu.'
8. Yosefe ndi Mariya ayenera kupita ku Betelehemu.
9. Ici ndi cifuniro ca Kaisara Augusto.
10. Ndi ulendo wautali umene ayenda.
11. Mariya akhala pang'ono kuona mwana!
12. Pothera afika m'Betelehemu.
13. Yosefe ndi Mariya ndi otopa cifukwa ca ulendo, koma kulibe malo kumene angagone.
14. Ndipo mwana adzayenera kubadwira kuti?
15. Atafuna-funa nthawi yaitali apeza malo: m'khola la ng'ombe.
16. Umu ndiye m'mene Ambuye Yesu abadwira.
17. Mariya amuka Yesu m'nsalu
18. Nam'goneka modyera ng'ombe.
19. Yosefe ndi Mariya ndi okondwera kwambiri.
20. Mulungu alonjeza Mwana uyu.
21. Ngakhale kwa Adamu ndi Hava.
22. Adzapulumutsa anthu ku macimo ao.
23. Onani, ndani awa?
24. Ndi abusa. Asamalira nkhosa. Ngakhale usiku.
25. Mwadzidzidzi abusa aona kuwala kwakukulu.
26. Ndi mngelo wocokera kuMwamba.
27. 'Ndibweretsa uthenga wacimwemwe cacikulu', atero mngelo
28. 'Ambuye Yesu wabadwa. M'khola la ng'ombe ku Betelehemu.
29. Agona modyera ng'ombe woikidwa m'nsalu.'
30. Mwadzidzidzi muli angelo ambiri m'mlengalenga.
31. Aimba: Ulemerero kwa Mulungu ndi mtendere pansi pano.
32. Cimveka bwino kwambiri!
33. Abusa ankhosa anena: 'Bwerani, tiyeni kwa Ambuye Yesu.'
34. Afika pakhola la ng'ombe.
35. Ndipo apeza Yosefe, Mariya ndi Mwana.
36. Abusa ankhosa atamanda Ambuye Yesu.
37. Abusa alikufalitsa uthengawu paliponse.
38. 'Ambuye Yesu wabadwa, M'khola la ng'ombe ku Betelehemu.'
39. Koma anthu sakhulupirira ici.
40. Yosefe ndi Mariya acoka m'khola la ng'ombe.
41. Afuna nyumba m'Betelehemu.
42. Ndiye kumene Yosefe, Mariya ndi Ambuye Yesu adzakhala.

Nthano iyi ipezeka mu Luka 1. 26-38 ndi Luka 2. 1-21

Phunziro 38 – Kuwerenga ndi kulemba

1. Yang'anani pa nchito yao ya kunyumba ndipo fotokozani malembo ndi masilabi omwe awabvutitsa

2. Uzani aphunzi kulemba mau awa pa bolodi

Ambuye, phiri, mtanda, mngelo, kumwamba, manda, Atate, mapewa

3. Werengani pamodzi pepala Phunziro 38. Ngati simukhoza kuwatengera pepala ilo, lembani ziganizo pa bolodi ndipo werengani pamodzi ndipo lolani aphunzi kuzilembanso m'mabuku ao.

4. Tsirizani phunziro pa kuimba nyimbo

Nchito ya kunyumba: Ikani zizindiko pa mau obvutitsa a pa pepala Phunziro 38

Phunziro 38

1. Asirikali ali kutsogolera Ambuye Yesu.
2. Apita ku phiri la Golgota. Komweko Yesu adzayenera kumwalira.
3. Yesu wanyamula mtanda waukulu wopangidwa ndi matabwa.
4. Mtandawo ulemera kwambiri pa mapewa ake.
5. Wina wace ali kubwera. Dzina lake ndi Simoni.
6. Mwadzidzidzi asirikali agwira Simoni. Iwo anena, 'Nyamula mtanda wa Yesu.
7. Cifukwa lye sangapitirize kuunyamula.' Iwo afika pa phiri la Golgota.
8. Simoni aika mtanda uja pansi.
9. Kenaka cinthu coipitsitsa kwambiri cicitika.
10. Asirikali akhoma misomali yaikulu m'manja ndi mapazi a Ambuye Yesu.
11. Imvani cimene Ambuye ali kulankhula.
12. Yesu apempherera adani ake. 'Atate, muwakhululukire iwo, pakuti sadziwa cimene acita.'
13. Cifukwa ca mazunzo ake Yesu akumva ludzu kwambiri.
14. Anena, 'Ndimva ludzu.' Msirikali mmodzi atenga cinkhupule.
15. Afikitsa cinkhupuleco ku kamwa kake. Motero Ambuye akhoza kumwako pang'ono.
16. Mazunzo akhala pang'ono kutha. Yesu ali pafupi kumwalira.
17. Koma asanafe lye afuna anthu onse kumvera cimene anena.
18. Apfuula ndi mau akulu, 'Kwatha!' Kenaka Yesu awerama mutu wake.
19. Sanyang'anyanso. Sapumanso. lye wamwalira.
20. Inde, tsopano lye wokondedwa wolowa m'malo walipira zonse.
21. Azimuna awiri ali kubwera. Maina ao ndi Nikodemo ndi Yosefe wa ku Arimateya.
22. Mosamala iwo acotsa mtembo wa Ambuye Yesu pa mtanda.
23. Yesu waikidwa m'manda aja.
24. Kenaka azimuna aja akunkhunizirapo mwala wolemara patsogolo pa dzenje lamdima.
25. Tsono Ambuye Yesu waikidwa m'manda.
26. Ndi mbandakuca. Dzuwa likalibe kutuluka. Mwadzidzidzi kumwamba kwatseguka.
27. Mngelo atsika. Wabvala cobvala cong'animira.
28. Mngelo apita ku manda. Akunkhuniza cimwala.
29. Manda ndi otseguka. Codabwitsa cacikulu ciri kucitika mu manda.
30. Ambuye Yesu abwereranso kukhala wamoyo. Auka.
31. Atuluka mu manda. Inde, iyo si nchito ya mngelo.
32. Koma ndi nchito ya lye mwini.
33. Popeza lye ndi Mwana wa Mulungu.
34. Komanso ndi nchito ya Atate wake. Popeza cilango catha.

Nthano iyi ipezeka mu Luka 23, Mateyu 27 ndi 28

Phunziro 39 – Kuwerenga

1. Yang'anani pa nchito yao ya kunyumba ndipo fotokozani malembo ndi masilabi omwe awabvutitsa

1. Werengani pamodzi pepala Phunziro 39 ndipo yankhani mafunso

Ngati simukhoza kuwatengera pepala, uzani aphunzi kutenga Baibulo ku phunziroli ndipo werengani pamodzi m'Macitidwe 2.4-12. Kenaka afunseni mafunso olembedwa muni.

Mayankho abwino ali conco:

1. Ndi kuti kumene ophunzira a Yesu anayenera kulalikra Mau a Mulungu?

Mu Yerusalemu

2. Ndi ciani cimene cinacitika pambuyo pace Ambuye Yesu adalangiza ophunzira ace?

Iye anawadalitsa ndipo anakwera kumwamba.

3. Ndi yani amene anaimirira pafupi ndi ophunzira?

Mngelo anaima pafupi ndi ophunzira.

4. Kodi angelo ananena ciani?

Iwo anati, "Ncifukwa ciani mukuyang'ana kumwamba? Iye wakwera, koma adzabwerera."

5. Angelo ananena kuti Yesu adzabweranso. Kodi mumayembekezera Yesu kubweranso?

Asiyeni ayankhe pa okha.

2. Ngati nthawi ilipo, uzani aphunzi kuwerenga nthano imodzimodzi m'magulu ang'ono.

3. Tsirizani phunziro pa kuimba nyimbo.

Nchito ya kunyumba: lembani nkhani ya banja lanu (tsamba limodzi)

Phunziro 39

1. Ambuye Yesu akhala pa dziko lapansi kwa nthawi yocepa.
2. Koma nchito ya Yesu ya pa dziko lapanso yatha.
3. Adzabwerera kumwamba posacedwa.
4. Kumwamba ndi nyumba yake yacifumu.
5. Uko ndi kumene lye anali kukhala lye asanabadwe m'Betelehemu.
6. Cifukwa lye ndi Mulungu.
7. Tsiku lina Ambuye ayenderanso ophunzira ake.
8. Iwo onse ali pamodzi m'Yerusalemu.
9. Ophunzira aja apita ndi Yesu pamene atuluka mu mzinda.
10. Pafupipo pali phiri. Ndi phiri la Azitona.
11. Ambuye Yesu alankhula ndi ophunzira ake.
12. Anena, 'Muyenera kupita konse-konse kudzaphunzitsa za ine.
13. Nchitoyo ndi yobvuta. Koma simudzayenera kuigwira pa inu nokha.
14. Atate adzatuma Mzimu Woyera. Iyenso ndi Mulungu.
15. Iwo afika pamwamba pa phiri la Azitona.
16. Onani, Ambuye Yesu ali kutambasula manja ake pamwamba pa mitu ya ophunzira. Awadalitsa.
17. Ndipo kenaka mwadzidzidzi Yesu watengedwa mu mlengalenga.
18. Wangonyamulidwa mopanda bvuto.
19. Ali kupita-pitabe mu mlengalenga. Ico ndi codabwitsa!
20. Ophunzira aja amuona lye ali kupita. Mwaulemu agwada pansi.
21. Amupembedza lye. Ophunzira aja akali cipenyenera.
22. Koma mwadzidzidzi akumva mau.
23. Pali azimuna awiri ali ciimirire pambali pao.
24. Azimunawo abvala zobvala za mtundu woyera.
25. Ndiwo angelo awiri. Mulungu wawatuma.
26. Inde, lye saiwala ophunzira ake.
27. Angelowo afunsa, 'Kodi cifukwa ndi ciani muyang'ana kumwamba?
28. Ambuye Yesu wapita kumwamba. Koma adzabweranso!'
29. Inde, tsiku lina Ambuye Yesu adzabweranso pa mitambo ya kumwamba.
30. Anthu onse adzamuona lye.
31. Ana ake onse adzakhala naye kumwamba.
32. Kodi nanga anthu ena onse?
33. Iwo adzalangidwa ku gehena. Sanatembenuke.
34. Ophunzira aja abwerera ku Yerusalemu.
35. Iwo ndi okondwa. Kodi inu mudziwa kuti cifukwa cace ndi ciani? 36. Cifukwa Ambuye Yesu akali pafupi nao.
37. Ico ndi cotheka popeza lye ndi Mulungunso.

Nthano iyi ipezeka mu Macitidwe 2.4-12

Phunziro 40 – Kulemba ndi kuwerenga – Nthano ya m'Baibulo

- 1. Congani nchito yao ya kunyumba ndipo konzani zolakwika**
- 2. Funsani aphunzi ngati ali ndi mafunso.**
- 3. Uzani aphunzi kulemba ndime iyi ya m'Baibulo m'mabuku ao.**
- 4. Macitidwe 2 ndime ya 4. Ndipo anadzazidwa onse ndi Mzimu Woyera, nayamba kulankhula ndi malilime ena, monga Mzimu anawalankhulitsa.**
- 5. Tengani mabuku ao ndipo konzani zolakwika zao**
- 6. Werengani pamodzi pepala Phunziro 40**
Ngati simukhoza kuwatengera pepala, lembani ziganizo 1-11 pa bolodi ndipo lolani aphunzi kuzilembanso m'mabuku ao.
- 7. Ngati nthawi ilipo, uzani aphunzi kuwerenga nthano imodzimodzi m'magulu ang'ono.**
- 8. Tsirizani phunziro pa kuimba nyimbo**

Nchito ya kunyumba: lembani nkhani imene inacitika m'mudzi mwanu

Phunziro 40

1. Muli anthu ambiri m'Yerusalemu!
2. Kuli anthu ngakhale ocokera ku maiko ena akutali.
3. Iwo onse apita ku kacisi kukapereka nsembe kuti aonge Ambuye.
4. Cifukwa Ambuye anawapatsa zokolola zabwino!
5. M'nyumba yapafupi ndi kacisi muli ophunzira a Yesu.
6. Iwo ali kupemphera pamodzi. Apempha kuti Mzimu Woyera abwere.
7. Mwadzidzidzi akumva cinthu cina.
8. Kuli kumveka ngati mphepo yaikulu.
9. Anthu amene ali kunja kwa nyumbayo akumva ico.
10. Kodi ico citanthauzanji? Onani!
11. Pamwamba pa mitu ya ophunzira pali malawi onga amoto ang'ono!
12. Imvani! Ophunzira ayamba kulankhula. Onani nkhope zao.
13. Iwo aoneka okondwa kwambiri.
14. Kodi cacitika ndi ciani?
15. Mzimu Woyera wabwera! Wabwera mu mitima ya ophunzira.
16. Anthu sakhoza kuona kubwera kwake ndi maso ao.
17. Koma akhoza kuona zizindikilo za kubwera kwa Mzimu Woyera.
18. Ndi nthawi ya Pentekoste.
19. Imvani! Ophunzira ali kuphunzitsa za Yesu.
20. Iwo alibenso konse mantha monga anali nao kale!
21. Kodi inu mukumbukira kuti iwo anakhoma zitseko cifukwa ca mantha?
22. Koma tsopano iwo saopa munthu wina aliyense.
23. Ici ndi codabwitsa ca pa tsiku la Pentekoste.
24. Anthu ena aseka ophunzira aja.
25. Iwo anena, 'Azimunawo amwa vinyo wambiri. Iwo ndi oledzera.'
26. Koma Petro anena kwa iwo, 'lai!
27. Sindife oledzera. Koma Mzimu Woyera wabwera.
28. Monga momwe Mulungu analonjeza m'Baibulo.'
29. Petro anenso cina, 'Munamupacika Ambuye Yesu.
30. Anthu ambiri amvetsera mwakacete-cete.
31. Iwo alaswa mtima. Akumva cisoni kwambiri.
32. Azindikira chimo lao lalikulu. Anapha Mwana wa Mulungu!
33. Ndipo lye ndi Mpulumtusi! Inde, anthuwo ndi osanyogodola.
34. Cifukwa Mzimu Woyera walowa mu mitima yao.
35. Ici ndi cifukwa cakuti iwo akumva cisoni.
36. Mzimu Woyera ndi wamphamvu kwambiri kuti anasintha anthuwo!
37. Inde, lyenso ndi Mulungu.

Nthano iyi ipezeka m'Macitidwe 2

Phunziro 41 – Kuwerenga Baibulo *Pemphero la Ambuye*

- 1. Congani nchito yao ya kunyumba ndipo konzani zolakwika**
- 2. Funsani aphunzi ngati ali ndi mafunso**
- 3. Werengani pamodzi pepala Phunziro 41a**
Ngati simukhoza kuwatengera pepala, uzani aphunzi kutenga Baibulo ku phunziroli ndipo werengani pamodzi Mateyu 6.5-18
- 4. Ngati nthawi ilipo, uzani aphunzi kulemba mau awa pa bolodi**
monga, woipayo, cifukwa, cakudya, mukhululukira, kwabwino, adziwa, pempherani
- 5. Tsirizani phunziro pa kuimba nyimbo**

Nchito ya kunyumba: Werengani Pepala 41b ndipo ikani zizindikiro pa mau obvutitsa a pa pepala Phunziro 41b
Ngati simukhoza kuwatengera pepala, uzani aphunzi kuwerenganso Mateyu 6.5-18 ndiponso kulemba mau obvuta a m'ndime izi m'mabuku ao.

Phunziro 41a

Mateyu 6.6-15

6. Koma iwe popemphera, lowa m'cipinda cako, nutseke citseko cako, nupemphere Atate wako ali m'tseri, ndipo Atate wako wakuona m'tseri adzakubwezera iwe.
7. Ndipo popemphera musabwereze-bwereze cabe iai, monga amacita anthu akunja, cifukwa ayesa kuti adzamvedwa ndi kulankhula-lankhula kwao.
8. Cifukwa cace inu musafanane nao: pakuti Atate wanu adziwa zomwe muzisowa, inu musanayambe kupempha lye.
9. Cifukwa cace pempherani inu comweci: Atate wathu wa Kumwamba, Dzina lanu liyeretsedwe.
10. Ufumu wanu udze. Kufuna kwanu kucitidwe, monga Kumwamba comweco pansi pano.
11. Mutipatse ife lero cakudya cathu calero.
12. Ndipo mutikhululukire mangawa athu, monga ifenso takhululukira amangawa anthu.
13. Ndipo musatitengere kokatiyesa, koma mutipulumutse kwa woipayo.
14. Pakuti ngati mukhululukira anthu zolakwa zao adzakhululukira inunso Atate wanu wa Kumwamba.
15. Koma ngati simukhululukira anthu zolakwa zao, Atate wanunso sadzakhululukira zolakwa zanu.

Malongosoledwe a Mateyu 6.6-15

1. Pamene Yesu anaphunzitsa ophunzira ake kupemphera, lye anati kuti ayenera kunena, 'Ufumu wanu udze' (Mateyu 6.10).
2. Kupempherera Ufumu wa Mulungu ndi kofunikira kuposa kupempha cakuda, zobvala kapena cina cimene tisowa.
3. Kupempha kuti Ufumu wa Mulungu udze ndi pemphero lalikulu loposa.
4. Ndipo Yesu anati kuti tikaika Ufumu wa Mulungu kutsogolo, tidzapatsidwa zina zonse zomwe tifunika. Ici ndi lonjezo lake!
5. Kodi tipempha ciani pamene tiika Ufumu wa Mulungu kutsogolo?
6. Tipempha Mulungu kutipangitsa ngati kuunika kakang'ono kwabwino kowalira kwa lye.
7. Tipempha kuti Mulungu adalitsa atumiki ake kuti anthu ena ambiri adzayamba kukonda Yesu.
8. Tipempherera atsikana ndi anyamata osadziwa Mulungu ndi kucita zinthu zoipa.
9. Kodi mungaganizire zinthu zina zimene tingapemphe Mulungu?
10. Tsaiwale pemphero lofunikira loposa: Ufumu wanu udze.

Phunziro 41b

Salimo 100

1. Pfuulirani kwa Yehova, inu, dziko lonse lapansi.
2. Tumikirani Yehova ndi cikondwerero: Idzani pamaso pace ndi kumyimbira mokondwera,

3. Dziwani kuti Yehova ndiye Mulungu; Iyeyu anatilenga, ndipo ife ndife ace; Ndife anthu ace ndi nkhusa za pabusa pace.
4. Lowani ku zipata zace ndi ciyamiko, Ndi ku mabwalo ace ndi cilemekezo: Myamiken; lilemekezeni dzina lace.
5. Pakuti Yehova ndiye wabwino; cifundo cace cimamka muyaya; Ndi cikhulupiriko cace ku mibadwo mibadwo.

Malongosoledwe a Salimo 100

1. Kodi mwathokoza Mulungu lero pa zabwino zonse zimene akupatsani?
2. Pamene Mulungu analenga Adamu ndi Hava, Iye anawaika m'munda wooneka bwino.
3. Kunali zinthu zambiri zooneka bwino m'munda kuwakondweretsa.
4. Koma Adamu ndi Hava anacimwa, monga mudziwa. Sanamvere Mulungu.
5. Kenaka Mulungu anakhoza kuwauza 'Simuyenera kukhala ndi zinthu zooneka bwino. Ndidzakucotserani zinthu zonse zooneka bwino'.
6. Koma Mulungu sanalankhule tero.
7. O inde, anacotsa Adamu ndi Hava m'munda. Ndipo anawauza kuti ayenera kugwira nchito molimba.
8. Anawauza kuti kudzakhala mbeu zosafunika ndiponso minga zimene zidzawabvutitsa. Anawauza kuti iwo adzakhala ndi cisoni ndi kuwawa.
9. Koma Mulungu anasiya zinthu zambiri zabwino ndi zokondweretsa kwa iwo kuti anakhoza kukondwerabe pang'ono.
10. O, Mulungu anali wabwino kwa iwo.
11. Ndipo Mulungu ndi wabwino kwa ifenso.
12. Atipatsa zinthu zambiri kutikondweretsa.
13. Pamene tiganiza za zonse zimene Mulungu atipatsa, tifuna kumkonda kwambirimbiri.
14. Tifuna kumyamikira ndi kumlemekeza.
15. Mulungu afuna kuti tizimyamikira ndi kuzimlemekeza.
16. Afuna kuti tizimkonda. Akondwa ndi kusangalala pamene timkonda.
17. Cimwemwe ceniceni ciripo cabe pamene tiyesa kusangalatsa Mulungu ndi kumkonda koposa.

Phunziro 42 – Kuwerenga Baibulo *Mfarisi ndi wamsonkho*

2. **Yang'anirani pa nchito yao ya kunyumba ndipo aphunzitseninso mau owabvutitsa**
3. **Werengani pamodzi pepala Phunziro 42 ndipo yankhani mafunso**
Ngati simukhoza kuwatengera pepala, uzani aphunzi kutenga Baibulo ku phunziroli ndipo werengani pamodzi Luka 18.9-14. Kenaka afunseni mafunso olembedwa munsu.

Mayankho abwino ali conco:

1. **Ndi anthu awiri otani amene anapita kunka ku kacisi? Ndi m'ndime izi mwapeza yankho?**
Mfarisi ndi wamsonkho (ndime ya 10)
2. **Kodi iwo anapita ku kacisi kukacita ciani? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?**
Anapita ku kacisi kuphemphera (ndime ya 10)
3. **Kodi mfarisi anapempha ciani? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?**
Mfarisi sanapemphe ciriconse. Anangofotokozera zabwino zake zambiri. (ndime ya 11-12)
4. **Ndi cifukwa ciani pemphero lake ndilo pemphero loipa?**
Sanazindikire kuipa kwa mtima wake. Iye anali wonyada.
5. **Kodi wamsonkho anapempha ciani? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?**
Anapempha cifundo (ndime ya 13)
6. **Ndi cifukwa ciani pemphero lake ndilo pemphero labwino?**
Iye ananena zonse kwa Mulungu moona mtima. Iye sanali wonyada.
7. **Kodi Mulungu amayankha pemphero lotani?**
Mulungu amayankha mapemphero oona mtima.

4. Tsirizani phunziro pa kuimba nyimbo

Nchito ya kunyumba: Werenganinso pepala Phunziro 42 kukonzekera mayeso a m'phunziro 43
Ngati simukhoza kuwatengera pepala, uzani aphunzi kuwerenganso Luka 2.1-15 kuti akonzekere mayeso a m'phunziro 43.

Phunziro 42

1. Azimuna awiri ali kupita ku kacisi. Apita kukapemphera m'nyumba ya Mulungu.
2. Ico ndi cabwino. Ico ndi cimene Ambuye afuna.
3. Mmodzi wa azimunawo ndi Mfarisi. Saiwala konse kupemphera.
4. Waimirira pa bwalo lalikulu la kacisi.
5. Anthu onse akhoza kumuona.
6. Akhozanso kumva zimene iye akamba.
7. Anena, 'Ambuye, ndikuyamikani. Popeza si ndine woipa monga anthu onse ena. Ndimacita zabwino zambiri.'
8. Iye aganiza kuti mtima wake ndi wabwino.
9. Ico ndi cifukwa cakuti iye sapempha mtima watsopano.
10. Aganiza kuti alibe macimo. Iye ndi wonyada.
11. Iye ndi wodzikuzza. Nanga mwamuna wina ali kuti?
12. Ali ciimirire kothera kwa kacisi. Koteru anthu samuona.
13. Iye akumva manyazi kwambiri. Cifukwa anacita macimo ambiri.
14. Mwamunayo ndi wamsonkho. Koma wamsonkho ndi wakuba.
15. Inde, iye anakhala woipa umoyo wake wonse.
16. Koma tsopano kodi? Tsopano iye akumva cisoni pa izo.
17. Ndinacitira anthu zoipa. Koma ndinacimwiranso Ambuye.
18. Ndipo ico ndi coipitsitsa koposa.
19. Iye ali kunena zonse kwa Mulungu moona mtima.
20. Mwaulemu apempha, 'O, Mulungu, mundicitire cifundo, ine wocimwa.'
21. Ico citanthauza: 'Ambuye ndinacita zoipa zambiri. Ndiyeneradi cilango. Koma conde mungandikhululukire macimo anga kodi?'
22. Mwamuna uyu apempheradi kwa Ambuye.
23. Mfarisi ndi wamsonkho onse awiri abwerera kwao. Wamsonkho wocitidwa cisomo!
24. Kodi nanga Mfarisi? Ambuye sanamuuze ciriconse.
25. Popeza Mfarisiyo sanapemphe cikhululukiro ca macimo ake.
26. Kodi ife timapemphera bwani?

Luka 18.9-14

9. Ndipo anatinso kwa ena amene anadzikhulupirira mwa iwo okha kuti ali olungama napeputsa onse ena, fanizo ili.
10. Anthu awiri anakwera kunka kukacisi kukapemphera; winayo Mfarise ndi mnzace wamsonkho.
11. Mfarisiyo anaimirira napemphera izi mwa yekha, Mulungu, ndikuyamikani kuti sindiri monga anthu onse ena, opambapamba, osalungama, acigololo, kapenanso monga wamsonkho uyu;
12. Ndisala cakudya kawiri sabata limodzi; ndipereka limodzi la magawo khumi la zonse ndiri nazo.
13. Koma wamsonkhoyo alikuima patali sanafuna kungakhale kukweza maso kumwamba, komatu anadziguguda pacifuwa pace nanena, Mulungu, mundicitire cifundo, ine wocimwa.
14. Ndinena ndi inu, anatsikira kunyumba kwace woyesedwa wolungama uyutu wosati uja ai; pakuti yense wakudzikuzza yekha adzacepetsedwa; koma wodzicepetsa yeka adzakulitsidwa.

Mafunso:

1. Ndi anthu awiri otani amene anapita kunka ku kacisi? Ndi m'ndime izi mwapeza yankho?
2. Kodi iwo anapita ku kacisi kukacita ciani? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
3. Kodi mfarisi anapempha ciani? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
4. Ndi cifukwa ciani pemphero lake ndilo pemphero loipa?
5. Kodi wamsonkho anapempha ciani? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
6. Ndi cifukwa ciani pemphero lake ndilo pemphero labwino?
7. Kodi Mulungu amayankha pemphero lotani?

Phunziro 43 – Mayeso ndi sewero

1. Uzani aphunzi kulemba mau awa m'mabuku ao

Macimo, pemphero, Mulungu, kacisi, Mfarisi, cisomo, akumva, khumi, Ambuye, anthu, awiri, anapita, mwapeza, amavankha

2. Tengani mabuku ao ndipo konzani zolakwika

3. Werengani pamodzi pepala Phunziro 43a.

Ngati simukhoza kuwatengera pepala, uzani aphunzi kutenga Baibulo ku phunziroli ndipo werengani pamodzi Mateyo 14.13-21

4. Uzani aphunzi kukhala m'magulu ang'ono a anthu awiri kapena atatu kuti awerenge pepala Phunziro 43b ndiponso kulemba bwino ziganizo mogwiritsa nchito mau osowa.

Ngati simukhoza kuwatengera pepala, uzani aphunzi kutenga Baibulo lao ku phunziroli ndipo werengani pamodzi Mateyu 8.1-13 ndipo onetsetsani kuti aphunzi amvetsa zimene awerenga.

5. Tengani mapepala ao ndipo konzani zolakwika

6. Tsirizani phunziro pa kuimba nyimbo

Nchito ya kunyumba: Pezani mau onse a pa pepala Phunziro 43c

Ngati simukhoza kuwatengera pepala, uzani aphunzi kulemba nkhani ya ku cipatala (tsamba limodzi)

Phunziro 43a

Mateyu 14.13.21 – Yesu acurukitsa mikate poyamba paja.

13 Ndipo Yesu pakumva, anacokera kumeneko m'ngalawa, kunka ku malo acipululu pa yekha; ndipo makamu, pamene anamva, anamtsata lye mumtunda kucokera m'midzi.

14 Ndipo lye anaturuka, naona khamu lalikuru la anthu, nacidira iwo cifundo, naciritsa akudwala ao.

15 Ndipo pamene panali madzulo ophunzira ace anafika kwa lye, nanena, Malo ano nga cipululu, ndipo nthawi yapita tsopano; kauzeni makamuwo amuke, apite ku midzi kukadzigulira okha kamba.

16 Koma Yesu anati kwa iwo, Iwo alibe cifukwa ca kumukira, apatseni ndinu adye.

17 Koma iwo ananena kwa lye, lfe tiribe kanthu pano koma mikate isanu, ndi nsomba ziwiri.

18 Ndipo lye anati, Mudze nazo kuno kwa lne.

19 Ndipo lye analamulira makamu a anthu akhale pansi pamaudzu; ndipo lye anatenga mikate isanuyo ndi nsomba ziwirizo, ndipo m'mene anayang'ana kumwamba, anadalitsa, nanyema, napatsa mikateyo kwa ophunzira, ndi ophunzira kwa makamuwo.

20 Ndipo anadya onse, nakhuta; ndipo anatola makombo otsala, mitanga khumi ndi iwiri yodzala.

21 Ndipo anadyawo anali amuna monga zikwi zisanu, kuwaleka akazi ndi ana.

Phunziro 43b

Lembani mau awa pa malo ao kuti ziganizo zimveke bwino.
cakudya - odabwa – udzu - anthu – wina - Ambuye – Yesu - adalitsa

Mikate isanu ndi nsomba ziwiri (Mateyu 14.13-21)

1. Onani, unyinji wa anthu awo!
2. Ali kumvetsera kwa Yesu.
3. Kuli kuda. Kodi anthu awa sapita kwao?
4. Ophunzira ake anena: 'Ambuye, atumizeni kwao.'
5. 'Ayenera apite kukadya.' Koma Ambuye sawatumiza kutali.
6. 'Adyetseni anthu,' Yesu anena.
7. Ophunzira aoneka..... Kodi ici cingatheke bwanji?
8. Pali anthu opitirira zikwi zisanu!
9. Kapena anthu awa akhala naco?
10. Inde, mnyamata m'modzi ali ndi cakudya.
11. Mikate isanu ndi nsomba ziwiri. Izi sizingakwane!
12. Anthu akhala pansu pa
13. Ambuye Yesu cakudya. Ndipo aduladula mkate.
14. Ophunzira angagawe izi.
15. Kodi mkate ndi nsomba zikwanira?
16. Inde, pali zokwanira aliyense.
17. Ndipo kuli zokhalira mataza khumi ndi awiri.
18. Anthu anena kwa mzake: 'Atidyetsa tonse. Kucokera ku mikate isanu ndi nsomba ziwiri.
19. Mphamvu yaikulu ya Ambuye Yesu!'

Phunziro 43c – Nchito ya kunyumba

Pezani mau onse.

M	I	K	A	T	E	A	C
R	V	M	T	A	C	R	A
N	S	O	M	B	A	I	K
A	N	T	H	U	N	Z	U
S	M	M	H	U	P	N	D
V	F	B	G	S	D	U	Y
B	O	L	U	E	G	H	A
A	P	P	U	Y	L	P	K
N	U	D	Z	U	E	O	Z

Pezani mau awa onse m'bokosi:

MIKATE
CAKUDYA
OPHUNZIRA
AMBUYE
YESU
NSOMBA
ANTHU
UDZU

Phunziro 44 – Kuwerenga Baibulo *Bartimaeus*

1. Congani nchito yao ya kunyumba ndipo konzani zolakwika

2. Werengani pamodzi pepala Phunziro 44 ndipo yankhani mafunso

Ngati simukhoza kuwatengera pepala, uzani aphunzi kutenga Baibulo ku phunziroli ndipo werengani pamodzi Marko 10.46-52. Kenaka afunseni mafunso olembedwa munsu.

Mayankho abwino ali concho:

1. Ndi cifukwa ciani Bartimeyu anakhala pansu m'mbali mwa njira? Ndi m'ndime iti momwe mwapeza yankho?

Yankho: Anali wopempha cifukwa anali wakhungu (ndime ya 46)

2. Kodi Bartimeyu anacita ciani pamene Ambuye Yesu anali pafupi? Ndi m'ndime iti momwe mwapeza yankho?

Yankho: Anapfuula (ndime ya 47)

3. Kodi anthu ambiri anafuna kuti Bartimeyu acite ciani? Ndi m'ndime iti momwe mwapeza yankho?

Yankho: Anafuna kuti aleka kupfuula (ndime ya 48)

4. Kodi Bartimeyu analeka kupfuula? Ndi m'ndime iti momwe mwapeza yankho?

Yankho: Sanaleke (ndime ya 48)

5. Nanga inu mucita ciani pamene anthu ena afuna kuti muleka kudalira pa Yesu yekha?

Yankho: Aliyense ayankhe pa yekha

6. Kodi Ambuye Yesu anacita ciani kwa Bartimeyu? Ndi m'ndime iti momwe mwapeza yankho?

Yankho: Anamcitsa (ndime ya 52)

7. Kodi tingaphunzire ciani m'nthano iyi?

Yankho: Aliyense ayankhe pa yekha

3. Uzani aphunzi kulemba ndime iyi ya m'Baibulo m'mabuku ao

Salimo 146 ndime ya 8. Yehova apenyetsa osaona; Yehova aongoletsa onse owerama; Yehova akonda olungama.

4. Tengani mabuku ao ndipo konzani zolakwika

5. Tsirizani phunziro pa kuimba nyimbo

Nchito ya kunyumba: Lembani nkhanu ya kulima (tsamba limodzi). Uzani aphunzi kutenga Baibulo ku phunziro 45.

Phunziro 44

Marko 10.46-52 - Bartimeyu wakhungu

46 Ndipo iwo anafika ku Yeriko; ndipo m'mene lye analikuturuka m'Yeriko, ndi ophunzira ace, ndi khamu lalikuru la anthu, mwana wa Timeyu, Bartimeyu, wopempha wakhungu, anali kukhala pansi m'mbali mwa njira.

47 Ndipo pamene anamva kuti ndi Yesu wa ku Nazarete, anayamba kupfuula, ndi kunena, Yesu, Inu Mwana wa Davide, mundicitire ine cifundo.

48 Ndipo ambiri anamuyamula kuti atonthole: koma makamaka anapfuulitsa kuti, Inu Mwana wa Davide, mundicitire cifundo.

49 Ndipo Yesu anaima, nati, Mwitaneni. Ndipo anaitana wakhunguyo, nanena naye, Limba mtima; nyamuka, akuitana.

50 Ndipo iye anataya copfunda cace, nazunzuka, nadza kwa Yesu.

51 Ndipo Yesu anamyankha, nati, Ufuna kuti ndikucitire ciani? Ndipo wakhunguyo anati kwa lye, Raboni, ndilandire kuona kwanga.

52 Ndipo Yesu anati kwa iye, Muka; cikhulupiriro cako cakupulumutsa iwe. Ndipo pomwepo anapenyanso; namtsata lye panjira.

Mafunso

1. Ndi cifukwa ciani Bartimeyu anakhala pansi m'mbali mwa njira? Ndi m'ndime iti momwe mwapeza yankho?
2. Kodi Bartimeyu anacita ciani pamene Ambuye Yesu anali pafupi? Ndi m'ndime iti momwe mwapeza yankho?
3. Kodi anthu ambiri anafuna kuti Bartimeyu acite ciani? Ndi m'ndime iti momwe mwapeza yankho?
4. Kodi Bartimeyu analeka kupfuula? Ndi m'ndime iti momwe mwapeza yankho?
5. Nanga inu mucita ciani pamene anthu ena afuna kuti muleka kudalira pa Yesu yekha?
6. Kodi Ambuye Yesu anacita ciani kwa Bartimeyu? Ndi m'ndime iti momwe mwapeza yankho?
7. Kodi tingaphunzire ciani m'nthano iyi?

Phunziro 45 - Mayeso

- 1. Congani nchito yao ya kunyumba ndipo konzani zolakwika**
- 2. Funsani aphunzi ngati ali ndi mafunso**
- 3. Fotokozani kuti m'Baibulo: $a = a$ and $g = g$**
- 4. Uzani aphunzi kutsegula Baibulo lao (Salimo 121)**
- 5. Uzani aphunzi aliyense kuwerenga ndime imodzi ya m'Salimo 121.**
- 6. Tsirizani phunziro pa kuimba nyimbo**